28-Pamene Lameki anali ndi zaka 182, anabereka mwana wa mamuna.

29-Ndipo anati, “Mwana ameneyu ndi amene atipumitse ife ku ntchito yathu yotopetsa, yolima mu mthaka imene anayitemberera Ambuye.” Ndipo anamutcha dzina lake Nowa.

32-Nowa ali ndi zaka zoposa 500, anali ndi ana atatu amuna, Semu, Hamu, ndi Yafeti.

-Dzina la chidzukulu cha Metusela linali Nowa.

-Tidzaphunzira za Nowa ndi ana ake amuna mu phunziro lotsatilalo.



PHUNZIRO LA 15

1. Kodi ndi ndani yekha amene amapereka moyo kwa anthu onse?
-Mulungu.

2. Kodi Kayni ndi Abele anabadwira kuti?
-Kunja kwa munda wa Edeni.

3. Kodi chifukwa chiyani Kayini ndi Abele anabadwira kunja kwa munda wa Edeni?
-Chifukwa chakuti bambo awo, Adamu, ndi mayi awo, Hava, anachimwa ndipo sanamumvere Mulungu.

4. Kodi chifukwa chiyani anthu onse anabadwira kunja kwa munda wa Edeni?
-Chifukwa chakuti bambo awo, Adamu, ndi mayi awo, Hava, anachimwa ndipo sanamumvere Mulungu.

5. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anakondwera ndi Abele ndikulandira msembe yake?
-Chifukwa chakuti Abele anamumvera Mulungu.
-Chifukwa chakuti Abele anabweretsa nkhosa ngati msembe kwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Abele anapita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu.

6. Kodi Abele amkadziwa chiyani za iye yekha?
-Abele anadziwa kuti anabadwira mu uchimo.
-Abele anadziwa kuti ayenera kulandila chilango cha imfa.

7. Kodi Abele anadziwa chiyani za Mulungu?

-Abele anadziwa kuti Mulungu ndi oyera.
-Abele anadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Abele anadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.

-Abele anakhulupiliranso zakuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye ku machimo ake.

8. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamukana Kayini pamodzi ndi msembe yake?
-Chifukwa chakuti Kayini sanamumvere Mulungu.
-Chifukwa chakuti Kayini sanabweretse nkhosa ngati msembe kwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Kayini amkayesa kupita kwa Mulungu mu njira yake, osakhala ya Mulungu.

9. Kodi Kayini amkaganiza chiyani za iye?
-Kayini samkaganiza zakuti anabadwira mu tchimo.
-Kayini samkaganiza zakuti tchimo lake liyenera kulandira chilango cha imfa.

10. Kodi Kayini amkaganiza chiyani za Mulungu?
-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu ndi oyera.
-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumpulumutsa iye.
-Kayini samkaganizanso zakuti iye akufunika Mpulumutsi kuti ampulumutse iye ku tchimo lake.

11. Mulungu atakana msembe ya Kayini, kodi chifukwa chiyani Mulungu analankhula ndi Kayini?



onse, Mulungu akhoza kuchita chimene akufuna kwa anthu onse.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga Enoki, Enoki amkamumvera Mulungu, Mulungu anamutenga Enoki kupita naye kumwamba.

-Enoki sanafe.

-Enoki asanafe, Mulungu anamutenga Enoki kupita naye kumwamba.

-Enoki ndi munthu yekhayo amene sanafe, Mulungu anamutenga iye kupita naye kumwamba.

-Dzina la mwana wa Enoki linali Metusela.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 5:25-27

25-Pamene Metusela anali ndi zaka 187, anabereka mwana dzina lake Lameki,
26-ndipo anakhalanso ndi moyo zaka zina 782. Anaberekanso ana ena amuna ndi akazi.
27-Anamwalira ali ndi zaka 969.

-Mwana wa mamuna wa Enoki, Metusela, anakhala nthaŵi yayitali kwambiri pa dziko la pasi kuposa munthu wina aliyense.
-Metusela anakhala ali moyo kwa zaka 969.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 5:28-29 ndi 32.

-Kodi kumwamba ndi kotani?
-Kumwamba ndi ku malo okongola kwambiri kumene kulibe kudandawula kapena kulira.
-Kumwamba ndi ku malo kokongola kwambiri kumene kulibe kudwala kapena imfa.

-Kumwamba ndi ku malo kumene Mulungu ndi angelo ake akukhala.

-Kodi ambiri a inu munayamba mwapitako ku Lilongwe (ku likulu la dziko lino)?
-Iyayi.

-Ngakhale kuti ambiri mwa inu simunapiteko ku Lilongwe, Lilongwe ikanalipobe.

-Ngakhale kuti ambiri mwa inu simunapiteko kumwamba, kumwamba kukanalipobe.

-Kodi kumwamba kuli kuti?
-Kumwamba ndi ku malo kwakutali kwambiri kuposa ku malo kumene kuli dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutengera Enoki kumwamba?
-Chifukwa chakuti Enoki amkamumvera Mulungu.
-Chifukwa chakuti Enoki anapita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu yekha.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga anthu onse, Mulungu ndiye mwini wa anthu onse.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga anthu



-Chifukwa chakuti Mulungu amkamukonda Kayini.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti Kayini alape tchimo lake.

12. Kodi Kayini anamumvera Mulungu?
-Iyayi.

13. kodi Kayini anamumvera ndani?
-Kayini anamumvera Satana.

14. Kodi Kayini anachita chiyani?
-Kayini anakwiya kwambiri, ndipo anamupha mng'ono wake, Abele.

15. Kodi Mulungu anaziwona zimene anachita Kayini?
-Inde.
-Mulungu amawona ndipo amazidziwa zinthu zonse.

16. Chifukwa chakuti Kayini sanamumvere Mulungu, kodi Mulungu anachita chiyani?
-Mulungu anamuthamangitsa Kayini.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:16-19 ndi 23

16-Chomcho kayini anachoka pa maso pa Ambuye Mulungu nakakhala m'dziko lotchedwa Nodi, kuvuma kwa Edeni.
17-Kayini anakhala pamodzi ndi mkazi wake ndipo anatenga pathupi, nabereka mwana dzina lake Enoki.
18-Enoki anabereka mwana namutcha kuti Eradi. Eradi anabereka Mehuyaele. Mehuyaele anabereka Metusela amene anabereka Lameki.
19-Lameki anakwatira akazi aŵiri. Dzina la mkazi

wake woyamba linali Ada, la mkazi wake wachiŵiri linali Zila.

23-Tsopano Lameki anawawuza akazi akewo kuti' "Iwe Ada ndi iwe Zila, mverani mawu anga. Tcherani makutu kuti mumve, inu akazi anga.
Ine ndapha munthu chifukwa chakuti anandipweteka .
Ndamuphadi mnyamatayo chifukwa chakuti anandimenya.

-Kayini anakana kumumvera Mulungu.
-Kayini anamumvera Satana yekha.
-Zidzukulu za Kayini nazonso zinatsata chitsanzo cha Kayini.

-Zidzukulu za Kayini nazonso zinakana kumumvera Mulungu.
-Zidzukulu za Kayini nazonso zinamumvera Satana yekha.

-Zidzukulu za Kayini nazonso zinakana kutsatira njira ya Mulungu.
-Zidzukulu za Kayini nazonso zinatsatira njira yawo.

-Ngati mmene Kayini anamuphera mng'ono wake, Abele, chimodzi mwa chidzukulu cha Kayini, Lameki, nayenso anapha munthu.

-Chifukwa chakuti Kayini anakana kumumvera Mulungu, zidzukuli za Kayini nazonso zinatsata chitsanzo cha Kayini, ndipo nazonso zinakana kumumvera Mulungu.

-Ndikofunika kwambiri kwa ife tonse kuti tizimumvera Mulungu.



ndi Hava.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira mu tchimo.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira mu imfa.

-Kodi Enoki amkadziwa chiyani za Mulungu?
-Enoki amkadziwa zakuti Mulungu ndi oyera.
-Enoki amkadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Enoki amkadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene anali oyenera kumupulumutsa iye.

-Enoki amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu kwa Satana.

-Enoki amkawawuza anthu ena kuti adzikhulupilira mwa Mulungu.
-Koma anthu ambiri amkakana kumumvera Enoki.

-Anthu ambiri amkakana kukhulupilira mwa Mulungu.

-Tsiku lina, chinthu china chake chodabwitsa chinamuwonekera Enoki.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 5:24

24-Enoki anali munthu oyanjana ndi Mulungu pa moyo wake onse; ndipo sanawonekenso chifukwa chakuti Mulungu anamutenga.

-Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Enoki?
-Mulungu anamutenga Enoki ndikupita naye kumwamba kukakhala ndi Iye.

-Chifukwa chakuti Adamu sanamumvere Mulungu koma anamumvera Satana.

-Hava nayenso anafa.

-Kodi Chifukwa chiyani Hava nayenso anafa?
-Chifukwa chakuti sanamumvere Mulungu koma anamumvera Satana.

-Pachiyambi, kunalibe imfa pa dziko la pasi pano.

-Mulungu samkafuna kuti Adamu ndi Hava kuti afe.
-Mulungu samkafuna kuti wina aliyense kuti afe.

-Adamu ndi Hava anafa chifukwa cha tchimo lawo.

-Chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa.

-Mulungu tsopano amatiwuza nkhani ya chidzukulu cha Seti M'buku Lake, chotchedwa Enoki.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 5:22-23

22-Enoki anabereka Metusela, ndipo anakhala ndi moyo zaka zina 300, akuyanjana ndi Mulungu. Anaberekanso ana ena amuna ndi akazi.
23-Anamwalira ali ndi zaka 365.

-Ngakhale kuti Enoki anabadwanso ali ochimwa, Enoki amakhulupilira mwa Mulungu ndiponso kumumvera Iye.

-Kodi Enoki amkadziwa chiyani za iye?
-Enoki amkadziwa kuti anabadwa ali mwana wa Adamu



-Ngati sitizimumvera Mulungu, ana athu nawonso atsata chitsanzo chathu, ndipo nawonso adzakana kumumvera Mulungu.

-Kayini ndi zidzukulu zake samakhala ndi za Mulungu.

-Kayini ndi mkazi wake amkangokhala mosangalala ndi za pa dziko la pasi, ndalama ndi ndi chuma chambiri.

-Tisamakhulupilire ndalama ndi chuma.
-Ndalama ndi chuma sizidzatipulumutsa ife.

-Mulungu yekha ndi amene angatipulumutse ife.

-Mulungu yekha ndi amene angatipulumutse ife ku mphamvu ya Satana.

-Chifukwa chakuti kayini anamupha Abele, Mulungu anamupatsa Adamu ndi Hava mwana wina.

-Adamu anamutcha mwanayo dzina lakuti Seti.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:25

25-Adamu anakhalanso pamodzi ndi mkazi wake, Hava, ndipo anatenga pathupi ndi kubereka mwana. Ndipo Hava anati, "Mulungu wandipatsa mwana wolowa mmalo mwa Abele amene anaphedwa ndi Kayini uja." Mwanayo anamutcha dzina lakuti Seti.

-Kodi mukukumbukira kuti Adamu ndi Hava atachimwa m'munda mwa Edeni, Mulungu analonjeza zotumiza

Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu kwa Satana?

-Mulungu anakhoza zotumiza Mpulumutsi kupitila mu mtundu wa Abele chifukwa chakuti Abeleyo amkakhulupilira mwa Mulungu.

-Koma Satana anamukakamiza Kayini kuti amuphe Abele.

-Satana anamukakamiza Kayini kuti amuphe Abele chifukwa chakuti samkafuna kuti Mulungu atumize Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu kwa Satanayo.

-Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, kodi Satana anamuletsa Mulungu kuti achite zimene amkafuna kuchita.
-Iyayi.

-Palibe amene angamuletse Mulungu kuchita zimene wafuna kuti azichite.

-Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, kodi Mulungu analiyiŵala lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Mulungu sayiwala malonjezo lake.

-Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, Mulungu anakhoza zotumiza Mpulumutsi kupitila mu mtundu wa Seti.

-Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, Mulungu anakhoza zotumiza Mpulumutsi kupitila mu mtundu wa



Seti kuti adzaŵapulumutse anthu kwa Satana.

-Nthaŵi zonse Mulungu amamaliza ntchito yimene wayiyamba.

-Palibe amene angamuletse Mulungu.
-Ngakhale Satana sangamuletse Mulungu.

-Seti anakula ndipo anakwatira.
-Mkazi wa Seti anabereka mwana wa mamuna.

-Anamutcha dzina lake Enoshi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:26

26-Seti anabereka mwana wa mamuna , ndipo anamutcha dzina lakuti Enosi. Pa nthaŵi imeneyo, anthu anayamba kutama dzina la Ambuye m'mapephero.

-Mulungu amatiwuza M'buku Lake kuti pamene mwana anabadwa kwa Seti, banja la Seti linayamba kutchula dzina la Mulungu ndi kukhulupilira mwa Iye.

-Patapita zaka zambiri Adamu anafa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 5:4-5

4-Seti atabadwa, Adamu anakhala ndi moyo zaka zinaso 800. Ndipo anaberekanso ana ena amuna ndi akazi.
5-Adamu anafa ali ndi zaka 930.

-Kodi chifukwa chiyani Adamu anafa?